


KUOMBOLEDWA KWATHUNTHU

 Ndinali ngati wosadziwa choti ndinganene m'mawa uno. Ndinakhala kumbuyo uko ndi M'bale Egan ndipo ndinamva...M'bale Neville amalankhula chinthu china ndikumapenya komwe kunali ine, ndipo ndinati kwa M'bale Egan, "Kodi akuyitana ine?"

Ndipo iye anati, "Kumene."

² Ndiyeno ndine ndiri pano kuti ndilankhule kanthu kena m'mawa uno. Ndimaganiza pamene ndinali... Chobweretsa mphepochi chikulanda mawu, chingokhala ngati chikumachotsamo pamene ukulankhula ndipo zikukhala ngati chobweretsa mphepochi chikungotengeratu mawuwa. Ndinali kumva maumboni pamene ndinali uko kupempherera mkazi pa foni, ndipo amene analandira uthengawo anaiwala kuikapo mzinda ndi malo komwe angawaimbire, a Dokotala akazi a Morrison. Ndipo ndingokamba chimene ndachita kaamba ka mapemphero anu nonsenu, ndi anga, ndinasanjika manja anga pa telefoni ndi kuloza pa nambala mosadziwa kuti ndi yakuti, ndi kupempha Mzimu Woyera kuti upite kwa mkaziyo. Chotero ndikuganiza Iye akanakhoza kumva zimenezo chimodzimidzi ndi momwe Iye akanachitira ngati tikadakhala ife...Mukuona? Ndipo ndinangoyiika pansi. Ndipo ziyenera kuti zachitika choncho momwe Ambuye amafunira. Mwaona? Mwina zingakhale kuti zikanakhala bwino chotero.

³ Ndiyeno ndinamva maumboni pamene ndinali mkatimo. Wina akunena kuti Mlongo Rook anali... Ine ndikukhulupirira ndi M'bale Neville amene anati kuti mlongoyo anali ndi—ubongo wake wasokonezeka, ngati. Tiyeni tinyamulire kwa Mulungu kuti zimenezo, tingokumbukira chinthu chimodzi ichi, Mulungu amadziwa Ake Omwe. Iye akudziwa zonse za iwo.

⁴ Kodi mukutha kumva bwino nonse kumbuyoko? Ngati simungathe, pali malo ena osakhalidwa kuno, mungathe kusintha ngati mukufuna kutero. Ndipo, tiyeni tiwone, kodi ichi ndi cholankhulirapo chachikulu? Ichi chiri kuno ndicho cholankhulirapo chachikulu? Chabwino. Tiwona ngati tingathe kuchiyandikitsa pafupi pang'ono. Bwanji nanga pozungulira chakuno, Gene? Apo zikhala bwino ndithu. Ndipo nthawi zina ndimangosasa mawu pang'ono pokha. Ndakhala ndikulalikira kwambiri...Kodi izo ziri bwinoko? Kodi mukutha kumva bwinoko?

⁵ Ndipo ife ndithudi tikukumbukira zimenezi mu pemphero. Ndipo tikufuna kukufotokozerani za msonkhano wa ulemerero wa kumusi mu...Kodi ine ndikuyang'ana pa Mlongo Rook? Ndimaganiza ndimayang'ana pa dona wina kumbuyoko amene

akufanana ndi iye. Ndinaganiza, “Ndithudi, ine sindikulankhula pawiri apa.” Ine ndikuyang’ana pa winawake amene amafanana ndi iye, chakumbuyo uko. Iye ali m’Chipatala cha ku Edward Woyera.

⁶ Ndipo chotero ku Cleveland, Tennessee, ndiponso mu California, tinali ndi misonkhano yaulemerero. Ambuye anatalitsa kopambana, ndi zinthu zambiri zimene Iye anachita. Ndipo tiri okondwa chifukwa cha zimenezo. Takondwa kukhoza kubwereranso kugulu lathu lomwe, kudzakufotokozerani za ubwino ndi chifundo cha Mulungu. Umo ndi momwe ankachitira m’Baibulo.

⁷ Ndimayamikira M’bale Neville...kapena pemphero la M’bale Beeler, momwe iye amapempherera anthu, ndi—ndi kupempha chithandizo ndi chifundo. Ngati ife titati tizingoyang’ana motsatira, inu nthawi zonse, chirichonse momwe chikuyendera, mudzapeza kuti pali chinthu china chowona chenicheni cha izo. Ndiyeno pamene M’bale Neville anabwera ndi madikoni awa kuguwa kuno, kuti—kuti adzapempherere madalitso a Mulungu pa—zopereka za mpingo, ndinamva iye akulankhula mupemphero lake kwa Mulungu za amuna awo, ndi momwe iwo amapemphererana wina ndi mzake. Ndipo izo zimandichitira ine ubwino kumva m’busa amene angapempherere madikoni ake, ndi madikoni kupemphereranso m’busayo. Pamene muona mpingo ukupita mu chigwirizano chotere, pamenepo, china chatsala pang’ono kuchitika. Umu ndi momwe mpingo uyenera kukhalira mu dongosolo. Ndipo zikungondipatsa ine lingaliro la choti ndilalikire. Ndimati ndilankhule za dalitso la pa Kadeshi, ndi za kukana kumvera lipoti la azondi, komano ndasintha malingaliro anga ku chinachakenso chotero.

⁸ Ndipo tsopano pa zokhudza machiritso, ndiri ndi kaumboni kena kamene ndikufuna kupereka. Ndinali mu chiyembekezo kuti ndimuwona m’nyamata wanga, Billy, kumbuyo uko, koma iye ali nazo mthumba lake. Ndipo Billy wayamba kuchita bwino mmisonkhano kusiyana ndi momwe ankachitira kale. Anali ndi manjenje ndi kukhumudwa, ndipo iye ankawauza anthu monga ngati kuti, “O, pitani kakhaleni pansi, pitani mukakhale pansi.” Namati, “Ine—ine ndikupatsani khadi la pemphero.” Koma ndaona posachedwapa kuti pakumakhala anthu mu msonkhano amene akuwamvera chisoni chabe, ngati alibe makadi apemphero otsala, ndiye amangowayika iwo m’chipinda kotero kuti ndikhoze kupita kukawapempherera.

⁹ Ndipo chinthu choterecho chinachitika ku Chicago nthawi yapitayo, ndipo ndikanafuna nditawerenga kalatayo ngati iye abwera muno. Sindinathe kumuwona iye ayi. Iye sanadziwe kuti ndimabwera m’mawa uno, mpaka kuno, ndi kufuna—kuifuna kalatayo. Koma ndinangoiganizira pamene ndinaganiza za matenda ochuluka choterewa. Ndipo umu ndi momwe

iliri. Ndi kalata yovomerezedwa imene ndinali kuwerenga mu pepala (sindinawerenge; ndinachita kuuzidwa), kuti pamene mu mapepala amamudzudzula Oral Roberts pomupempherera mkazi amene adali ndi nthenda ya shuga ndipo anamwalira. Ndipo ine, osati kuchokera mu...monga Wachimerika, ine—ine ndimakonda kumvera malamulo ndi—ndi munthu amene ali mu ulamuliro, koma ndikuganiza kuti icho sichilungamo. Nkudabwa ngati angalolere kulemba mu pepala onse amene Oral Roberts anawapempherera nachiritsidwa, amene madotolo anawalephera nawasiya. Ndikudabwa ngati angatembuzire mbali inayo kamodzi, mwaona. Iwo sangachite zimenezo. Ndipono ndikuganiza kuti mwina Mdierekezi wangowaphimba iwo m'maso chotero, kuti, ndipo Mulungu akungololera, kuti Tsiku Lachiweruzo iwo adzakhale ndi yankho kwa icho. Koma ndikudziwa za anthu zikwi amene Oral Roberts anawapempherera, amene anali kufa, ndipo iwo alibwino.

¹⁰ Kotero inu mukuona, iwo, ali okondera pa ichi. Iwo amapereka mbali imodzi, mbali yotsutsa, koma sangapereke mbali inayo. Tsopano, pepala iyenera kumauza anthu nthawi zonse pa zomwe zikuchitika kumene. Ndiye ndikuganiza ngati anthu akamakhudzidwa ndi za wina ndi mzake, ngati wina achiritsidwa, kuchiritsidwa kwenikweni, pepala iliyonse mu Amerika inayenera kumalemba nkhaniyo. Koma simungawapange hayala n'komwe kuti achite zimenezo. Ayi, mukatumiza china ngati chimenecho kumeneko, iwo akaziyang'ana monyodola ndi kuziseka nazibweza, koma tsopano ngati pali china choti achitsutse. Zikungowonetsa kuti fuko lino liri lokonzekera chiweruzo. Ndichoncho. Ndipo payenera pakhale chiweruzo, ndipo palibe njira yochithawira icho, ndipo iwo akungodziunjikira moto pa mitu yao, ndi zina zotero, ndi monga—kusagwirizana pa zolinga. Pepala, cholinga chake ndi kuti—azifotokozera anthu za chinthu chirichonse chabwino kapena choyipa chimene chikuchitika. Koma iwo ali kutali ndi zolinga zawo. Ndipo pamene ali kutali ndi zolinga zawo, ndiye iwo—iwo sazitumikira zolinga zawo moyenera.

¹¹ Ndipo umu ndi momwe ziliri ndi mpingo. Pamene mpingo uli kutali ndi zolinga zake, iwo sungathe kutumikira oyer mtima ake bwino. Tiyenera kukhala pamodzi, tiyenera kukhala ogwirizana. Tiyenera kukhala a mtima umodzi ndi a chiyanjano chimodzi. Kapena, sitidzatha kutumikira Mulungu kapena anthu pokhapokha titakhala a mtima umodzi ndi chiyanjano chimodzi, kuti tiyime ndi zolinga za Baibulo ndi zinthu zimene Mulungu anati zimenezo ndi zoyenera. Tiyenera nthawizonse kuima nazo.

¹² Billy anatsala m'chipinda ku Chicago, iye...Winawake anafika kwa iye, anali mkazi ndi mwamuna wake, ali ndi khansara wa m'mapapo, akufa, ndipo mkazi wakeyo anali wogwidwa ndi polio ali mu chikuku, ndipo mkaziyo akuyesetsa

kumasamalira mwamunayo amene ankalephera ndi kuyima komwe, ndi khansara m'mapapo ake. Ndipo Billy anati kwa iye, anati, "Pe—pepani, bwana." Anati, "Ndikadakonda kukupatsani khadi yapemphero." Ndipo iye anati, "Koma ine—ine ndiribe yina yomwe yatsala."

¹³ Ndipo bamboyo anati, "Chabwino, zonse ziri bwino, mwana wanga." Iye anati, "Zonse ziri bwino." Nati, "Tinayesetsa kufika kuno, koma zinali zotivuta kwambiri ife."

¹⁴ Billy anati, "Ndikuuzani zomwe mungachite." Naati, "Ndipita kukawatenga bambo ndipo ndilowa nawo muno, ndipo ine ndituluka nawo." Ndipo anati, "Ndikatero, pamene inu mudzakhala mutamvera uthenga wao," anati, "ndiye inu muwatenge...kapena akazi anu ndi inu, ndipo mudzalowe mkachipinda uko kumene ine nditi ndidzadzereko, ndipo ndidzawachititsa kuti akupempherereni."

¹⁵ "O," iye anati, "umenewo ndi ulemu, mwana wanga. Izo nzabwino mokwana." Mukuona? Apa pali—pali khalidwe, onani. "Ndi zabwino mokwana. Izo ziri bwino." Mwaona?

¹⁶ Ndipo usiku umenewo, Billy, pamene anapitanso kumeneko, akutsutsanabe ndi zomwe ananena, pakuti anali ndi mulamu wake momwemo amene anali ndi matenda otuluka magazi m'mapapo, ndiponso mulamu wake wamkazi amene ankatuluka magazi mmimba chifukwa cha nsungu, amenenso analowa pamodzi nawo, zowoneka mwa mbali ya kuwathandiza iwo kuti alowe. Muyenera kuwonetsetsa, kukanakhala chipinda chonse chodzaza, mukuona. Koma popita mwakudutsa ndi kuwapempherera iwo, tinalandira imodzi ya makalata yonena kuti bambo uja anachiritsidwa kwathunthu ku khansara ya mmapapo ija; mkazi ujanso, mkazi wake mu chikuku, akuyenda bwino bwino mopanda chovuta monga momwe analiri kale; bambo yemwe ankatuluka magazi mu—mu mapapo, ndi chifuwa chachikulu, alibwino kwathunthu, ndipo mkazi wake wachira zironda za m'mimba. Anayi a iwo kuchiritsidwa molunjika! Ndikudabwa ngati manyuzipepala angalole kulemba zimenezo. Mwaona? Mwaona? O, koma Mulungu adakali Mulungu. Iye amangochita zinthu mwa njira ya Iye Mwini, mukudziwa, ndipo Iye ndi wabwino chotero. Tiri okondwa kudziwa kuti Iye ndi Mulungu.

¹⁷ Tinkalankhula mmawa wina za mlaliki wina wamng'ono amene tikumudziwa kuti anakakonda kupita kukapempherera odwala ndi chirichonse, ndipo iye anapita kukapempherera munthu kuchipatala cha mu Louisville, ndi wa chifuwa chachikulu, mayiyo anamwalira. M'nyamatayu anati, "Chabwino, nkosafunika...Mulungu sali...Kulibe Mulungu, Iye bwenzi atasunga Mawu Ake" Naati "Ine ndinamudzoza iye monga momwe—momwe Baibulo limanenera. Ngati Iye sasunga Mawu Ake, Iye siMulungu ayi." Anati, "Ndi Bukhu chabe."

18 Tsopano, izo zikanawoneka ngati zotero kupatula pamene umudziwa Mulungu. Limenelo ndi gawo la Malemba, koma siMalemba onse. Izi zimatengera chikhulupiro cha munthuyo payekha. Mwaona?

19 Ndipo ine ndinamuza mkazi wanga, ndinati, “Pakhala zinthu zambiri zomwe zachitika, zimene ndikungodziwa kuti ziripo. Sindikudziwa chimene chidzachitika kwa ine potsiriza. Mwina ndidzapita mwa njira yomweyo. Ngati Mulungu asuntha dzanja Lake lachifundo kwa ine, ndidzayenda njira yomweyo. Koma momwe Iye ati asiyire dzanja Lake la chifundo nanditsogolera, ine ndipitirirabe.” Koma ndinamufunsa Meda, ndinati, “Ndi ndani anali mchipinda m'mawa uja nditatha kuona masomphenya a msungwana wanga wamng'ono, Sharon?”

20 Pajanso, tsiku lina, ndinali ngati ndikomoka, ndinali nditakhala ku msewu. Ndipo mukudziwa nkhani yonse ya masomphenya a iye pamene. . . Ndipo ndinayang'ana, kubwera mbali yomwe ndinali, ndipo kumeneko kumadza msungwana wamng'ono mumsewu konkuno ku Jeffersonville, zinali chimodzimodzi ndi masomphenya aja. Ine ndinangodzigwira manja anga pamodzi. Zinkawoneka kwambiri ngati masomphenya aja a msungwana wanga Sharon; apano anali mayi wocheperapo.

21 Ndipo atha masomphenya amenewo mmawa umenewo pamene ndinali mu Ulemerero, Ine. . . Hope anali kundiwuzwa ine, mikono yake atayangata pa phewa langa, kumati, “Usadandaule za ife Bill. Ife tiri bwinoko.” Ine ndinkayesa kuti ndingodzipha. Ndipo iye anati, “Usadandaule. Undilonjeze kuti sudzadandaulanso konse.”

22 Ndipo ine ndinati, “Sindingalonjeze zimenezo, Hope, chifukwa ine—ine—ine ndiri—ine ndikudandaula. Sindingachitire mwina.”

23 Ndipo ndinatuluka mu masomphenyawo, nditayimirira m'chipinda mwa mdima. Ndipo osakhala masomphenya, osati zolingalira, koma manja ake anali ali chiyangatiwe pa ine. Ndipo iye ankandisisita. Ndinaganiza, “Nditayembekezera kamphindi. Izi sikuti. . .” Sindinadziwe izo kuti ndizitche chiyani masiku amenewo, masomphenya, ine ndinawatcha chizimbwizimbwi. Ine ndinati, “Ndi ili. Dzanja lake linakali pomwepo.” Ine ndinati, “Kodi uli pompanobe, Hope?”

24 Iye anati, “Bill, undilonjeze kuti sudzadandaulanso za ine ndi Sharon.” Chifukwa ndinali pamapeto a msewu, ndinali wokonzeka kudzipha. Ndinati, “Ndikukulonjeza.” Pamenepo iye anandikupata nandisisita ndi dzanja lake. Ndiyeno ine—ine ndinati, “Hope, kodi uli kuti?” Ndinanyamuka. . . ndinawunguza mmwamba ndipo ndinagwira kaunyolo koyatsira magetsi ndikukakoka. Ndinazungulira, kufufuza mmipando

yonse kuti ndiwone ngati anali atakhala mmenemo. Ndi Mulungu. Iye adakali Mulungu lero chimodzimidzi ndi momwe Iye analiri pa Phiri la Kuwalitsidwa pamene Mose ndi Eliya anawonekera. Iye akanali Mulungu.

²⁵ Tikhoza kupyola mmavuto ndi m'mayesero ochuluka. Tangokumbukirani, pali Wina Amene amadziwa, amatiunikira njira, nachititsa iyo kukhala yeniyeni. Ine sindikudziwa chomwe chiri kuseri kwa katani, koma ndikudziwa chinthu chimodzi, ine ndikulimbikira kulinga ku malo a mayitanidwe opambana, tsiku lirilonse kuyesa kukhala moyembekezera chochitika chachikulu chimene chiti chidzachitike tsiku lina pamene nditi ndidzamuwone Iye maso ndi maso ndi kudzanana nthano ya kuwomboledwa mwachisomo. Limenelo ndilo tsiku lomwe ndikukhalira moyo. Kusiya zinthu zonsezo mmbuyo, zomwe ziri, ine ndikufuna kulimbikira, kumangopitirirabe.

²⁶ Ndikufuna Kachisi uno, tsopano poti inu mwayima chotere, ndikufuna inu mupitirize kulimbikira kumka ku malo a mayitanidwe opambana. Chirichonse chomwe muchita, mamatiranani pamodzi, mukhale ngati mbumba imodzi momwe mungathere kutero, koma nthawi zonse ndi dzanja lofuna kufikira ndi kutenga wina kuti mubwere naye mkati. Koma mu Chikhulupiriro ichi chomwe ife tikulalikira tsopano ndi kulimbanira modzipereka, musasunthe inchi imodzi kwa Icho. Pakuti, ngati inu mukukhulupirira kuti ine ndi wantchito Wake, ili ndi dongosolo la Mulungu! Sizidzakhala za mu gulu ayi. Nthawi zonse zidzakhala mu anthu ochepa, momwe zakhala zikuchitikira ndi momwe ziti zizidzakhala. Koma kumbukirani, kunalembedwa, "Musaope, nkhusa zochepa inu, ndi chifuniro chabwino cha Atate wanu kukupatsani Ufumu."

²⁷ Tsopano, pali gulu la audindo mu mpingo wathu uno, madikoni, matrasitii, oyang'anira za Sande sukulu, m'busa, munga momwe mpingo wathu unaikidwira mu dongosolo lake. Ndipo inu ndinu anthu amene munawasankha amauidindo amenewa ndi m'busa uyu. Ine ndine wongoyang'anira pa zonse, onani kuti zizipitirira bwino, ndi kupereka chilangizo ndi zina zotero. Inu ndi amene mumasankha m'busa wanu, mumasankha matrasitii anu, mumasankha madikoni anu, mumasankhira udindo uliwonse womwe uli mu mpingo uno, inu anthu. Ndipo ndi udindo wanu kuyima ndi anthu amenewo, onani, poti iwo akhoza kulakwitsa. Iwowa ndi anthu oti adzafa, iwo ndi anthu chabe, ndipo akhoza kulakwitsa. Koma ngati Purezidenti wa Amerika atalakwitsa, kodi ife timamuchotsa iye Upurezidenti? Timangoziwala zimenezo ndikumapitiriza. Ndi momwe tikufunira kuchita ndi mpingo wathu tsopano. Ndimamvera iye maminiti angapo apitawo, akupempherera madikoni, ndiponso kumva kumbuyoko umboni, pakhomopo, kuchokera kwa matrasitii, momwe nonse muliri a cholinga chimodzi. Tsopano khalani mwa njira imeneyo. Tsopano,

inu mamembala imani nawoni matrasitii awa, madikoni ndi m'busa. Ndipo kumbukirani, pamene muchita zonse palimodzi, kumbukirani kuti ndi ntchito ya Mdierekezi kuona kuti aziphwasule zimenezo. Tsopano chakhala chikuchitika ndipo nthawi zonse chidzakhala choncho. Koma inu muyime ndi a paudindo anu, ndipo icho ndi chimene ndimafuna kuchipanga.

²⁸ Ndipo ndiye ine ndiri ndi zinanso—kanthu kena koyenera pa bolodi la zolengeza m'mawa uno, za msonkhano wa gulu loyang'anirali ndi ulamuliro wawo. Ndipo icho chikhala pa bolodi la zolengeza, ndipo ine ndiri ndi china cha M'bale Roberson amene ali wapampando wa ma—wa matrasitii. Ndiponso ndiri ndi china cha M'bale Collins, ndikuganiza, amene ali ngati wapampando wa gulu la madikoni. Ndipo tsopano, maudindo onsewa akhazikidwa mwa Malemba, ndipo ayenera kukhala ndi mayendetsedwe ake mwa Malemba a zimene ayenera kuchita. Kotero, matrasitii ali ndi udindo waowao. Ndiponso Madikoni ali ndi udindo waowao. Oyang'anira Sande sukulu ali ndi udindo waowao. Ndipo m'busa ndiye mutu wa nkhosa zonse.

²⁹ Tsopano, uliwonse ndi woyanjana ndi unzake. Ndipo ine ndikuganiza kuti misonkhano yanu musamachitire pamodzi, koma muyenera kuchita audindo uliwonse pa okha, chifukwa madikoni alibe choti anganene kwa matrasitii pokhapokha atakhala ndi zochita zina zoti azipereke kwa iwo. Mbali inayonso choncho, matrasitii amayang'anira zachuma ndi zinthu za zomangamanga, iwo alibe kanthu kalikonse pa za madikoni. Madikoni ali ngati apolisi mu mpingo, ndi othandizira m'busa. Ndipo matrasitii ndi osamalira chuma chonse. Matrasitii alibe choti angachite mbali ya zauzimu, ndipo madikoni alibe choti angachite mbali ya za chuma. Kotero, izi zizitero. Ndipo oyang'anira Sande sukulu ndi amene ali pa za Sande sukulu. Kotero ndalebetsa zonsezi, zatayipidwa, kuti zizikhala pa bolodi la zolengeza.

³⁰ Ndiyeno tiyikanso mu feremu Chiphunzitso chomwe mpingo ukuyimira, ndipo tichipachika mu tchalitchi momwe muno; zomwe tikuyimira, m—mfundo, Chiphunzitso cha mpingo. Tsopano, kuti tikhale mpingo, tiyenera kukhala ndi Chiphunzitso.

³¹ Sitimangoyika chikhomo chirichonse ndi kunena, “Tizipita mpaka *apa* basi.” Timapita kutali mpaka poyanjana ndi aliyense amene Mulungu angatilore kupitako mwa Malemba Ake pochita ndi anthu. Ndipo tsopano mamatiranani, khalani a cholinga chimodzi, mtima umodzi, ndi kupitirira mwakumvera Mulungu. Imeneyo ndi njira yomwe Mulungu akufuna ife tidzichita. Tsopano tiyeni tipempHERE ndiyeno titsegule Mawu.

³² O Ambuye Opambana, tikuyandikira tsopano ku Mawu Oyera kapena kuwerenga kwa Mawu awa. Mulole Mzimu Wanu Woyera ukatimasulire chimene ife tikusowa. Ndipo

tiloreni tikalankhule, Ambuye, ndi kuchita ndi kukhala moyo, podziwa kuti tonse ndife ana Anu, mwa chisomo, momwe Inu munatiyitanira ife. Mutakhala chiyanjano mu mpingo uno, poona kuti tatsala pang'ono kufika mu kachitidwe kopambana, tikukhudzidwa, kuti tikuze alaliki ena kuti azipita ku minda kumene, ngati Inu mudzandituma kupitako, zigawo zosiyana za mdziko, kumeneko ndikakhazikitse Chikhulupiriro, ndi kuti tizikhala ndi mlaliki wokonzeka ndi wololera, ndi wophunzitsidwa kuti akapitirize. Ndipo mulole kuti Chikhulupiriro chomwe chinapatsidwa kamodzi kwa oyera mtima, chimene ife molimba mtima tikuyima nacho, chikazungulire dziko lonse. Tichitireni ichi, Ambuye. Ndipo tikupempha kuti kamphuthu kakang'ono ka udzu aka, monga zinaliri tsiku lina pamene tinakadalitsira kwa Inu, mulole kuti mpingo uyambe pano, Ambuye, kuti kuchokera pamenepa patuluke otumikira ndi alaliki ndi aphunzitsi ndi atumwi amene akafike ku zigawo zonse za dziko lapansi.

³³ Ife tikupempha, mmawa uno, madalitso apadera kwa M'bale ndi Mlongo Stricker amene akuvutika tsopano. Koma tikudziwa kuti tonse tikuyikidwa pa mayesero amenewa. Mwana aliynse amene adza kwa Mulungu ayenera kukwapulidwa, kuyesedwa. Ndipo ngati tigonja mophweka, ndi kubwerera m'mbuyo, ndiye ndife ana apathengo, ndipo osati ana a Mulungu. Muwapatse M'bale ndi Mlongo Stricker nyonga ndi mphamvu, kuti apitirize kuyima pa malo awo antchito. Ngati ziwatengera kumapempha chakudya, mukawatambasulire dzanja Lanu la madalitso pa iwo. Pakuti sitikudziwa koma mwina zikhoza kukhala kupyolera mu kulimbikira komweko kuti Inu mukhoza kuwaonetsa anthu a ku Afrika Chikhristu chenicheni kuti ndi chotani. Kwaniritsani ichi, Ambuye. Tsopano lolani kuti izi zonse zichitike mwakufuna Kwanu.

³⁴ Mudalitse m'busa uyu, M'bale Neville. Tikupemphera, Ambuye, kuti Inu mumupange iye kukhala m'busa wa nkhoza zanu, monga Inu mwachitira naye m'mbuyomu. Ndipo sitikuiwalanso mkazi wake wokondeka amene akudwala kwambiri. M'dani akufuna kumusiyira M'bale Neville gulu la ana ilo, opanda mayi, koma ife tikuima ndi kuyika, mwa chikhulupiriro, Mwazi wa Yesu Khristu pakati pa mdani ameneyo ndi mlongo wathu. Mulole Mzimu Wanu, Ambuye, kuti ukhale wopambana pa iye, podziwa kuti akazi onse kunapatsidwa kwa iwo kuti aziyenda kupyola mu chigwa chimenechi, cha m'dima wa m'badwo uno, koma tikupemphera kuti Inu mukhale naye. Muwadalitse ana ang'onowo. Mlongo wathu akhala wamanjenje tsopano, ndi woopsyedwa, koma mulole Mzimu Woyera ukhale pa khomo la chifundo nthawi zonse kwa banjalo.

³⁵ Dalitsani gulu la matrasitii athu, M'bale wathu Wood apo, ndi M'bale wathu Egan, M'bale Roberson, ndi ena onse,

Ambuye. Madikoni, matrasitii, ndi ena onse ochitira nawo pamodzi mu mpingo, tikupemphera, Ambuye, kuti muwalole iwo atumikire nthawi yawo ndi chiyero ndi—ndi chilungamo. Dalitsani iwo, Ambuye, amene agwira ntchitoyi m'mbuyomu. Ndipo tikupemphera kuti Inu mupitiriza kukhala nafe kuti tidzadziwika ngati mpingo wogwirizana ndi mzimu ndi chikondi cha Ambuye. Tikupemphera tsopano kuti Inu mugawe kwa ife Mawu mwa kusowa kwathu, pamene tikuwerenga kuchokera mu Mawu Anu olembedwa. Pakuti tikupempha izi m'Dzina la Yesu. Amen.

³⁶ Pakupemphera, ndimaganiza pamene timadalitsa kapena kupempha madalitso kwa atsopano athu...gulu lathu latsopano la matrasitii ndi ena otero, ndimaganiza za M'bale Fleeman ndi M'bale Deakman ndi iwo amene akhala pano, amene anatumikira bwino kale. Ndipo tikufuna kuthokoza kwa Mulungu chifukwa cha kutumikira kwao kodzipereka. Ambuye azikhala nawo nthawi zonse ndipo awadalitse iwo ndi kuwathandiza iwo. Ndikufuna kuwerenga tisana... Ingokumbukirani tsopano, bolodi ya zolengeza ndi zina zotero, ndi msonkhano umene ukudza.

³⁷ Ndipo tiri okondwa pokhala nafe m'mawa uno, chabwino, ndikhoza kunena motere, bambo amene wakhala wofunika kwambiri kwa ine m'nthawi zapitazo, ndiponso wofunika tsopano, m'bale wabwino, Fred Sothmann wochokera ku... ndi mkazi wake, ochokera ku Saskatchewan, Canada, amene wadzakhala nafe kuno pa ulendowu. Mu dziko lathu lino, wapaulendo; koma muchiyanjano chathu, m'bale wokonedwa, M'bale Fred Sothmann wakhala apoyo. Iye amasalira za misonkhano yanga pamene ndinali mu Canada.

³⁸ Ndi m'bale wina wofunika amene poyamba anali wa ku Canada, amene anali wabizinesi, ndipo akhoza kutsimikizira kwa dziko kuti simungathe kupereka kuposa momwe Mulungu amachitira. Iye ndi mzake anakhazikitsa thumba la ndalama zomangitsira malo, kapena ndalama za utumiki wa kumayiko ena, maziko. Ndipo iwo anandiitanira ine kumsonkhano wa ku Oakland, ndipo anati anali ndi ndalama, iwo anatilipirira zonse kuchokera mu thumba lawo la mazikolo.

³⁹ M'bale Fred ndi ine tinayesa kuti ndalama zina zimene M'bale Fred anali nazo kuti ndisazitenge ngati zanga zanga. Koteru tinaganiza kuti tizipereke kwa anthu a ku Canada ndi kuti tisadzitenge chopereka, koma sizinayende bwino chotero. Misonkhano inali bwino, koma chifukwa sitinatenge chopereka... Ziribe kanthu ngati mpingo uli wolemera madola mabilioni zana limodzi, muli ndi ngongole kwa Mulungu yoti mutenge chopereka. Limenelo ndi gawo la kupembedza. Ndipo inu mumaba zimenezo...Monga momwe ndakhalira wodana ndi ndalama ndi zinthu chotero, ndinazindikira kuti pamene munthu ulakwa uyeneranso kumavomereza kuti walakwa,

chifukwa M'bale Fred ndi ine taziwona palimodzi kuti sibwino kumene.

⁴⁰ Ndipo, M'bale Borders, pamene ndinamsiya M'bale Fred ndi kubwera kwa inu ku Oakland, ndinati “Musadzachite zimenezo. Muzingoyendetsa mbale yolandirira ndi kutenga chopereka, ndipo, kaya ndi zingati, kazisungeni mu thumba lanu la maziko lija zodzachitira msonkhano kwina.”

⁴¹ Ndipo msonkhano usanatsekedwe, M'bale Borders ndi anzawo anadza kwa ine nati, “Zonse zimene tinasungira—msonkhanowu, zatha kale.

⁴² Ndipo tsopano masiku angapo apitawo iye anakonza msonkhano ku San Jose, California, kumene iye anali ndi ina, ndiganiza, mipingo 60 kapena 70 mu chigwa chokhacho, onse a zikhulupiriro zosiyana atagwirizana. Tinali ndi msonkhano wodabwitsa, ndipo tibwererakonso mu Novembala. Tiri okondwa kuti inu muli nafe, M'bale Borders ndi M'bale Fred amene akhala kumbuyoko. Ndipo amuna amenewa ali. . . ndi alendo mwina kwa nonsenu, koma akhala ali abale ofunika kwambiri kwa ine kunja potumikira, kulimbanira moona Chikhulupiriro chimene ife taima nacho. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Tiri okondwa kukhala nanu mmawa uno mu Kachisi wamng'onoyu kuno; kulibe zoti mungaziyang'ane, koma pali chinthu china pano chimene tikudziwa ndicho kuti Mulungu amakhala pano, mukuona. Kotero tiri okondwa pa chimenecho. Ndipo pali abale enanso ofunika, ndikanakhala ndi nthawi yowatchula, amene ali nafe lero.

⁴³ Tsopano ndikuyembekezera ndi kupemphera kuti m'masiku ochepa akudzawa, Ambuye akalola, ndifuna kudzapita, ndikungoona kutsogozedwa, sindinalengeze zimenezi, msonkhano wotsatira, ku Ohio, kukakhala ndi M'bale Sullivan pa bwalo la misasa, posachedwapa. Ndi mitunda zana limodzi lokha kukafika kumeneko, ndikuganiza, Gene, pafupifupi choncho. Udzakhale ulendo wabwino ngati simunakonze kale tchuthi chanu, ngati Ambuye apitiriza kutitsogolera. Munthu wabwino kwambiri, ndipo tikuyamika M'bale Sullivan kwambiri. Kungoti, iye ndi mfumu ya mzinda, ndi amene anali mfumu ya mzinda, ndipo wachi Kentucky wachikaledi. Zimenezo ndi zomwe ndinganene za iye. Pamene ndinakumana naye tsiku lina mu. . . Tonse tinaleredwa ku mapiri a Kentucky, iye anati kwa ine, “Kodi ukadalibe ndi asafetida pakhosi lako, Billy?” Tsopano mukudziwa momwe—momwe iye aliri wachi Kentucky. Tsopano tiyeni tibwerere. . . Sindikunyojetsa konse abale anga a ku Kentucky amene ali pano, M'bale Jeffreys ndi ena otero. Ndine wachi Kentucky, inenso, mukudziwa. Ndikuuzani chinthu chimodzi chomwe tiri, ife sitiri achi Kentucky kapenanso Amerika ayi; ndife amwenda mnjira ndi alendo, tikufuna mzinda ukudzawo.

44 Tsopano mwa kuwerenga, tiyeni tiwerenge kuchokera m'Bukhu la Eksodo kwa maminiti angapo. Ndikufuna kuwerenga kuchokera pa mutu wa 23 ndipo ndime ya 20 mpaka 23, palimodzi. Ndipo ndikufuna kutenga phunziro ili m'mawa uno kuchokera pamenepa chotere, la izi, kani, *Kuomboledwa Kwathunthu*. Ndipo sindilankhula nthawi yaitali tsopano pamene ndikuyembekezera kuti mutsegule Bukhu lanu pa mutu umenewu.

Taona, Ine ndituma Mngelo akutsogolere iwe, kukusunga iwe panjira, ndi kukufikitsa pamalo pomwe ndakonzzeratu.

Musamalire iye, . . . mvera mawu ake, usamuwawitse mtima; pakuti sadzakhululuka zolakwa zako: popeza dzina langa liri mwa iye. (Ndikutsimikiza kuti mpingo ukumudziwa Mngelo ameneyo anali ndani) . . . dzina langa liri mwa iye.

Ndipo ngati umvera ndithu mawu ake, ndi kuchita zonse zimene Ine ndizilankhula; ndiye Ine ndidzakhala mdani wa adani ako, ndipo ndidzasautsa okusautsa iwe.

Pakuti Mngelo wanga adzakutsogolera iwe, nadzakufikitsa iwe . . . kwa Aamori, . . . Ahiti . . . Apezezi . . . Akanani, . . . Ahivi, ndi . . . Ayebusi: ndipo ndizawaononga.

45 Ambuye adalitse Mawu Awo pamene tikulankhula tsopano timaminiti tochepa, ngati mungamapemphere. Ndimaganizira za phunziro ili la *Kuomboledwa Kwathunthu*. Mpingo wakhala uli mu—mu kagulu kochepa. Nthawi zonse udzakhala, mwa mamembala, mpakana Yesu adzabwera. Koma iwo ukukhala pansu pa mwayi wopatsidwa ndi Mulungu. Tikanangodziwa, umenewu ndi Mpingo wa Mulungu wamoyo, osati Branham Tabernacle, pakuti Branham Tabernacle ndi gawo chabe la iwo. Aliponso makachisi ena otere mdziko monse muno.

46 M'bale Snelling usiku uno akhala ndi msonkhano wa ubatizo, ndinayiwalanso kuti M'bale Curtis anandiuza kuti ndilengeze zimenezo, kani amandiuza dzulo kuti akhala nao. Iye ali ndi msonkhano wa ubatizo, ndipo ngati wina pano sanabatizidwebe, bwanji, M'bale Snelling akakondwera kuchita zimenezo usiku uno. Uko ndi ku Holiness Tabernacle ku Utica. Ndiponso M'bale Junior Jackson ku New Albany. Ndipo kuli matchalitchi ambiri mdziko monse muno, koma tonse tikukhala, zikuwoneka ngati, mbali ya ogenjetsedwa, kwambiri kapena pang'ono.

47 Ndinamva M'bale Neville akulengeza m'mawa uno kumbuyo uko, chimenecho chakhala ngati chabwera mmalingaliro anga, kuti anthu akukhala ngati akuchokamo muchiombolo. Chikuwoneka ngati chiri chinthu china chimene anthu achiona

kotero iwo akungochikankhira kumbali imodzi, “O, chabwino, Mulungu akhoza kuchita icho.” Koma limenelo si khalidwe!

⁴⁸ Tsopano, Mose, pamene anaitanidwa ndi Mulungu, iye anali kwathunthu, m’neneri wathunthu. Pamene Mulungu atuma munthu kuti achite chirichonse, Iye amamupatsa zida zokwanira ndi chirichonse chimene iye angachifune. Ngati Mulungu aitana munthu kuti akhale mlaliki, Iye amayika chinachake mkati mwake kuti azilalikira nacho. Ngati Iye amuitana munthu kuti akhale mphunzitsi, Iye amayika chinachake mwa iye kuti aziphunzitsira nacho. Ngati Iye amuitana munthu kuti akhale m’neneri, Iye amaika chinachake mwa iye kuti aziwona masomphenya ndi kukhala m’neneri. Mulungu nthawi zonse mwathunthu amampatsa zida munthu Wake. Ndipo izo ndi zimene Iye anachita chabe pamene Iye anamtuma Mose ku Igupto. Anamulera iye mwa njira yina yake, ndipo Anamuphunzitsa iye mwa njira yina yake, ndipo Anamuumba ndi kumupanga iye ndi kumupatsa kachitidwe. Iye atamulonjeza Abrahamu, zaka mazana zisanachitike, kuti Iye adzawombola anthu, ndiye Iye—yaze mmaganizo ake anali ndi cholinga chodzamupanga Mose mwa njira imene Mose anapangidwira. Mose anali m’neneri wathunthu. Ndiyeno pokhala mneneri wathunthu...

⁴⁹ Ndiye monga inu chabe, ngati muli Mkhristu. Mulungu samapanga Mkhristu woperewera, Mulungu amapanga Akhristu athunthu. Mulungu samapanga alaliki operewera, koma mlaliki akhoza kukhala woperewera. Ndipo Mulungu amapanga ana ake Akhristu, koma nthawi zina iwo amakhala Akhristu operewera. Koma sicholinga cha Mulungu kuti iwo akhale chotero. Ndi njira zao zomwe azisakaniza ndi dongosolo lomwe Mulungu anali nalo pa moyo wao, ndipo izo ndi zomwe zikuwapangitsa iwo kukhala momwe ali. Mulungu safuna iwo kuti akhale Akhristu operewera kapena alaliki operewera, onyengerera mbali iliyonse. Kapena, Iye amafuna iwo ayime mwathunthu pakatikati!

⁵⁰ Tsopano, Mose, Mulungu anamupanga iye kukhala m’neneri wathunthu wa chiwombolo chathunthu. Ndipo Mose anadzipereka kwathunthu m’manja mwa Mulungu. Icho ndi chifukwa chomwe chinamupanga iye chomwe anali. Iye anali mwa Mulungu kwathunthu mpakana kuti Mulungu akanamudalira.

⁵¹ Ndikudabwa m’mawa uno, monga Akhristu, ngati tadzipereka chifuniro chathu, ndi kudzipereka tokha kwathunthu kwa Mulungu, mpakana kuti Mulungu akhoza kutidalira ife pamalo pamene Iye watiika. Ndikudabwa m’mawa uno, za inemwini, ngati ndikanakhala wodzipereka kwa Mulungu mpakana kuti Mulungu azindidalira, kukhoza kumudalira M’bale Neville, kukhoza kudalira gulu lathu la matrasitii, gulu lathu la madikoni, athu—mamembala athu a mpingo wathu. Ife tonse tiri ndi malo ndiponso tiri ndi udindo.

⁵² Mlaliki ali ndi malo a ntchito ya kuyimirira ndi kulalikira chuma chosapezeka wamba cha Khristu, mopanda kunyengerera, ngati anayitanidwa kuti akhale mlaliki. Iye sangalekerere kanthu kamodzi kwa munthu mmodzi ngati iye anayitanidwa kuti akhale mlaliki.

⁵³ Ndipo membala wa mpingo, iye wayitanidwa kuti akhale membala wa gulu limeneli, ndiye sayenera kunyengerera. Ngati mpingo ukukhulupirira kuti tisamachite juga, ndiye membala aliyense asamagwire mpukutu wa juga. Sitimakhulupirira zakumwa mowa, ayenera kuchotsa maganizo ake kotheratu pa zakumwa. Ngati ife sitikhulupirira kusewera juga ndi kusuta, membala wa mpingo uno asayesere kugwira chinthu choterocho. Mulungu amapereka chiwombolo chathunthu. Pamene ife...Iye adzachita izi ngati ife tidzipereka tokha mwathunthu kwa Iye. Ngati tidzadzzipereka mu dzanja Lake, ndiye Mulungu akhoza kukhala mwa ife, Khristu Chiyembekezere cha Ulemerero. Iye angadzionetse Yekha mwa ife ngati tidzichotsa patsogolo pake, ndiye zoganiza zathu zikhala zoganiza Zake. Kodi mungayerekeze Khristu akusuta chindudu? Kodi mungayerekeze Khristu akumwa mowa, kapena kusewera juga? Ndiye ngati mzimu wanu uli gawo limodzi la Mzimu Wake, Iye akufuna izi zikhale mwa kuvomereza kwanu. Koma inu mumalola Mdierekezi kuti alowemo ndikutenga ulamuliro, ndipo nthawi zonse mu mtima wanu pansu pomwe mwakuya mumadziwa kuti mukulakwa pamene muchita zinthu zimenezo. Ndipo pamene membala wina akhoza kulankhula zoyipisa membala wina; mukudziwa kumeneko nkulakwa. Munalamulidwa kuti muzipemphererana wina ndi mzake, osati kunenana wina ndi mzake, koma kukondana wina ndi mzake. Ndipo ngati wina agwa, tiyeni timudzutse, timuthandize. Tsopano, chimenechi chitipanga ife gu—gu—gulu logwirizana la okhulupirira. Tsopano, pamene sitimvera zimenezo, ndiye sitimvera Mulungu ndipo sitimkondweretsa Mulungu. Ndipo koteru mpingo wathu, anthu athu sangatukuke, mpingo sungapitirire, chifukwa tiri osagwirizana limodzi. Monga Yesu anati, “Chimera chochepa chimatupitsa mtanda wonse.”

⁵⁴ Tsopano, ngati gulu la mpingo, kapena monga—madikoni akanabwera ndikunena kuti ife timati...timaganiza kuti timange kachisi watsopano. Ngati imeneyo ili voti ya madikoni, ndipo matrasitii nawo amauzidwa ndipo ngati alibe ndalama zochitira izo, ndiye amapangana dongosolo la zomanga monga momwe takhala tikuchitira pakali pano. Ndiyeno zimaperekedwa ku gulu lonse, monga momwe tiyenera kukhalira, mpingo wonse pokhala woyima pawokha. Ndiye ngati mpingo uchitira voti kachisi watsopano, ndiye ife tonse tiyenera kugwirizana pamodzi mkumanga kachisi watsopano.

⁵⁵ Mosabisa, inemwini, pamene iwo ananena za kachisi watsopano kwa ine, ndinali wotsutsa ganizolo. Ndi choncho.

Ine ndinati “Sitikusowa kachisi watsopano kwenikweni. Mwina ndichoka kuno posachedwapa monga Ambuye. . . ngati zomwe Iwo anandiwonetsera zikwaniritsidwa. Ndi wa chiyani kachisi watsopano? Ife tiribe ndalama.”

⁵⁶ Ndiye ndinabwera kudzamva momwe mpingo ukukhudzidwira, kuti ambiri mu mpingo amaoneka kuti akufuna titero. Ndiye ine ndinachita chiyani? Ndinachotsa maganizo anga ndi kuvomerezana ndi mpingo. Zoonā, tiyeni tichite zimenezi, monga momwe achitira mayere. Umu ndi mmene zinaliri m’nthawi ya Baibulo, momwe mpingo unkachitira voti. Ku—kuyima patokha, magulu a anthu amakhala palimodzi. Mu umodzi muli mphamvu. Ndiye kotero ine ndinati, “Zedi, ngati umu ndi momwe mpingo ukufunira, ngati umo ndi momwe Mulungu akufunira, Iye ali ndi ulumuliro wambiri wochititsa voti pakati pa gulu lonse la anthu kusiyana ndi chomwe Iye ali nacho kwa ine, chifukwa ine ndiribe masomphenya kuti ndinene kuti zisakhale choncho. Kotero ife tigwirizane ndi mpingo, ndi kuchita palimodzi ndi mpingo. Ndipo ine ndiri pambuyo pa zonse kuchita momwe . . . ndingathere, mwaona, kuthandiza mpingo.

⁵⁷ Ichō chiyenera kukhala cholinga cha Mkhristu aliyense ndi munthu aliyense mu mpingo, ndiko kuti tigwirizane tokha ndi kumamatirana limodzi. Chirichonse chimene mpingo uvotera, ndi chimene tiyenera kuyima nacho. Ndiye titati, mwachitsanzo, iwo akafuna kusintha chinthu china mu mpingo. Chabwino, ndiye, ngati matrasitii atafuna kutero, kapena wina atafuna kutero, madikoni, iwo atafuna kusintha chinthu china, chimenecho amawuuzā mpingo, mpingo wonseno palimodzi. Ndipo ngati athu—ngati maganizo athu apa akuoneka osiyana pang’ono ndi chimene mpingo wonse ukuchita, tiyeni tichotse maganizo athu, chifukwa iyo ndi njira yokha yomwe ife tingayimire mogwirizana. Ndipo ngati mpingo uno udzangopitirira kuyenda mwa njira yomwe mukupita tsofano, ndi kukhala ogwirizana limodzi, Mulungu adza. . . Ndi zopanda malire zimene Iye adzachita ngati tumamatirana limodzi. Tiyenera kumamatirana limodzi. Umo ndi momwe tikufuna kuti tikhale, athunthu chotero kwa wina ndi mzake, ndiyeno chotero athunthu m’manja a Mulungu.

⁵⁸ Ndiyeno ife tiyenera kukhala ndi munthu amene tikumukhulupirira kuti amalalikira Mawu a Mulungu. Ngati munthuyu satero, ndiye tipeze wina amene angakhoze kutero. Umo ndi m’mene tiyenera kuyimira. Ngati gulu la matrasitii siliyimira chomwe chiri choyenera, ndiye ndi ntchito yanu kusankha wina amene angayimire chomwe chiri choyenera. Ndiye pamene muchita icho, muyime nacho. Ziri kwa inu. Imani nacho. Ndipo tonse limodzi tikuyimira Chinthu chimodzi, ndicho Mulungu!

⁵⁹ Ngati membala alakwitsa, osamutaya; muthandizeni, muyimikeni, khalani palimodzi, mumvetsetsane wina ndi mzake. Umu ndi momwe Malembo akunenera. Pamene tilakwitsa, tiyeni tipite pamaso pa Mulungu. Tisanapite pamaso pa Mulungu, tiyenera kupita kwa munthu amene tamulakwirayo.

⁶⁰ Ndinangochita zimene zija. Ndipo ndikudziwa kuti ndinalakwa, ndinanama, ndinamuchititsa mkazi wanga kunama. Ndikhulupirira ndinakuuzani za zimenezi kutchalitchi kom'kuno. Anali masiku angapo apitawo osati kale, ndi pafupifupi masabata asanu ndi limodzi apitawo. Ozenga milandu anali atandilemetsa ndi zofuza zawo mpakana sindimadziwa komwe ndinali. Ndinali nditangopita kunyumba kuchokera ku ofesi kukalandira chakudya cha madzulo, ndipo foni yangayanga inalira Meda napita kukayankha foniyo. Iye anayika dzanja lake pa iyo, nati “Ndi oweruza mirandu kanonso.”

⁶¹ Ine ndinati, “Sindingapirirenso usiku wina. Mutu wanga ndikungomva ngati ukusokonezeka. Malingaliro anga akutayika, kumangondikokera uku ndi uko ndi kuno.” Ine ndinati, “Sinditha kupirira nazo.” Ndipo ndinayamuka, ndi kuti, “Awuze kuti ine sindiri muno,” ndipo ndinathamangira kuseri kwa nyumba.

⁶² Pamene ndinabwerera, (Meda chikumbumtima chake chomwe sichimagwirizana ndi zinthu zimenezo), iye anakumana nane pa chitseko, atatsala pang'ono kulira, nati, “Bill, ndi zabwino zimene wachitazi?”

⁶³ Umadziwa momwe uliri. Ine ndimadziwa momwe ndiliri. Ndinati, “Zedi, ine sindinali m'nyumba muno nthawi imene ija.” Ndimadziwabe kuti Mulungu sanakondwere nane pakutero. Ndinati “Sindinali muno nthawi imene ija.

Anati, “Koma iwe unali mommuno pamene iye anachita telefoni.”

⁶⁴ Madzulo amenewo ine ndinapita kukapempherera mwana wodwala. Ndipo ndisanachoke kunyumba, telefoni inaliranso ndipo mwana wanga Joseph anathamanga nakagwira foniyo nati “Adadi, mukufuna ndiwauze kuti inu simuli muno?” Onanitu momwe tchimo limaonongera, lingadzakhale banja lotani limenelo potsirizira?

⁶⁵ 1 Yohane mutu 5 ndime ya 21 anati, “Ngati mitima yathu sititsutsa ife, ndiye kuti tiri ndi chodalira mwa Mulungu. Koma ngati mitima yathu ititsutsa, tingakhale bwanji ndi chodalira mwa Mulungu?” Ife tikudziwa kuti pamene tiri ndi tchimo limene liri losalapidwa, Iye sadzatimvera ife konse. Ndi zolimba zimenezo, koma, iwo—iwo—iwo, mpingo ukusowa zinthu zimenezi.

⁶⁶ Ndiye ndinayamba kupempherera mwanayo. Ndipo pamene ndinayamba kusanjika manja anga pa iye, Ambuye

anandidzudzula nati, “Iwe unanena bodza, iwe suli woyenera kupempherera mwana ameneyo.”

⁶⁷ Ndinapotoloka kuyamba kuchoka kwa munthuyo, ndinati, “Bwana, inu mungondiyembekezera pano. Ine ndiri ndi chinthu china choti ndikachikonze.”

⁶⁸ Ndinamuyimbira foni woyimira mirandu uja ndipo ndinapita ku ofesi, kumuyitanira m’menemo, ndipo ndinati, “Onani, bwana, ine ndinanena bodza. Ndinamuza mkazi wanga kuti aname, iye anati ine sindinali m’nyumbamo. Ndipo ine ndinangothawira kuseri kwa nyumba.” Ndipo ine ndinalapa ndi kumuza iye za izo.

⁶⁹ Iye anadza pafupi, nadzayika dzanja lake pa phewa langa, nati, “M’bale Branham, nthawizonse ndakhala ndiri ndi chidaliro mwa inu, koma ndiri nacho chopambana kuposa kale tsopano. Munthu,” iye anati, “amene ali wololera kukonza zolakwa zake!”

⁷⁰ Ndipo ine ndinamuza iye, ndinati, “Ndimayamba kupempherera mwana ndipo Ambuye sakanalola... zimangonditsutsa mu mtima wanga, chifukwa ndinadziwa kuti ndinalakwa.”

⁷¹ Ndiye tsiku lotsatiralo, mkazi wanga anati “Kodi ukupita kuti?”

Ine ndinati, “Ku phanga langa.”

⁷² Ndipo ine ndinapita ku phanga langa pamwamba pa Charlestown, kumene ndakhala ndikupita kwa zaka, ndipo ndinalowa m’menemo ndi kupemphera tsiku lonse. “O Mulungu, musadzandilorenso ine kuchita zinthu ngati zimene zija. Mundikhulukire ine, Ambuye, pakuti pamene ndinayamba kuyika manja pa anthu odwala kuti ndipemphere, pamenepo ndinatsutsika.” Cha mma 3 koloko madzulo ndinatulukamo, ndipo pali mwala waukulu umene uli pamenepo, ndipo ine ndinakwera pamwalapo ndipo ndinali ndikuyang’ana cha kummawa, manja anga ali m’mwamba, ndikuyamika Ambuye. Ndipo panangokhala zii pamenepo, ndipo ndinati, “Ambuye, ngati inu mutangoti...Nthawi ina Inu munadutsa pafupi ndi Mose, ndipo iye anati inali nthawi imene Inu munamulola iye kukhala m’phanga la thanthwe, ndipo unaonekera ngati msana wa munthu.” Ine ndinati, “Kodi Inu mungachichitenso, Ambuye, kuti ndidziwe kuti ndakhulukiridwa?” Ndipo ine ndinati, “Ngati Inu mudzandithandiza ine ndi kudza m’maganizo anga,” ndinati, “Ambuye, ine—ndiribe ubongo wamphamvu, chifukwa ndiribe maphunziro.” Ndinati, “Ndipo ine—ine ndikuyesetsa kukutumikirani Inu. Inu mukudziwa mtima wanga, ndipo ine sindinachite...Sindinayenere kuchita zimene zija. Sichinali cholinga changa kuchita zimene zija. Mutu wanga unangokhala ngati ukuchoka, ndinali wonjenjemera kwambiri, ndipo

ndinachita ichi mwa kanthawi kochepa pamene Satana anandigwira ine.” Ndinati, “Ngati Inu mwandikhulukira ine, ndiroleni ndikuwoneni Inu kotero, Ambuye.”

⁷³ Ndipo Mulungu pokhala Woweruza wanga, cha kumbali kwanga, pa kamalo kakang’ono pathengo panayamba monga kuzungulira kwa Mphepo, ndipo Iyo inadza kumbali ya phanga kumene ndinaliko, niipitirira kupyola mu nkhalango. O, m’bale, mtendere umene simungaumvetse unandizinga ine, ndipo ine ndinalira, ndinasisima, ndinafuula. Ndikudziwa machimo anga anakhulukidwa kwa ine. Onani, ine ndinachoka mu chilumikizano ndi Mulungu, sindikanakhala ndi chiwombolo cha kwa mwana uja.

⁷⁴ Ndipo tsiku lotsatiralo panali munthu wochokera ku Chicago, amene ali munthu wotchuka, wa Chikatolika amene anali atangotembenuka kumene, mavalavu a mkati mwa mtima wake anali atatupa ngati chubu, ndipo anali atayesera kuwadula kwa nthawi yaitali, amapitanso, ndipo iye sanawaloreze. Potsiriza anapeza mwayi woti ndikambirane naye. Ndikamalankhulana ndi anthu, timangokhala pa chimenecho mpakana titapeza chomwe chavuta. Ndipo munthuyo anangolowa mchipindamo ndipo nthawi yomweyo Mzimu Woyera unapita mmbuyo mu moyo wake nutchula china chimene iye anachichita pamene anali m’nyamata wothandizira paguwa mu mpingo wa Katolika. Iye anati, “Zimenezo nzoonadi. Zimenezo nzoonadi mosabisa.” Anati “Kodi ndiye mukutanthawuza kuti zinali mangawa kwa ine?”

Ine ndinati, “Umenewo ndi mdima wokha umene ndikuwuwona m’moyo wako.”

⁷⁵ Anapitanso nakawauza adotolo, nati, “Chabwino, tengani zinthu zonse pamodzi tsopano, tikhale nayo opareshoni.”

⁷⁶ Adotolo anati, “Tiyang’anenso mumtima.” Ndipo pamene anayang’anamo, iye anati “Inu simukusowanso kuchitidwa opareshoni.”

⁷⁷ Onani, “Ngati mitima yathu ititsutsa.” Tikusowa kuomboledwa kwathunthu. Sitikufuna kukhala mpingo woperewera. Tikufuna tikhale Mpingo weniweni, kapena pasakhale mpingo konse. Tikufuna tikhale Akhristu enieni, kapena tisakhale Akhristu konse. Tikufuna kuomboledwa kwathunthu ku zizolowezi zathu, ku machimo athu, ku kuganiza kwathu koyipa, ku mchitidwe wathu woipa, ku kusamala kwathu, chirichonse chimene tachichita. Tikusowa kuomboledwa kwathunthu, kotero kuti pamene anthu abwera mtchalitchi muno kudzapemphereredwa, kudzakhale kagulu kakang’ono aka, (mwina osapyola 100 kapena 200) katakhala muno, koma iwo adzakhale m’manja mwa Mulungu kwathunthu. Ndipo pamene tipemphera, ndiye Mulungu adzamva kuchokera Kumwamba. Mulungu akufuna wina

wake amene Iye angamugwire m'dzanja Lake, wina amene Iye angati, "Ine ndiri ndi chidaliro mmenemu. Ndikhoza kutumiza uyu, kapolo Wanga wodwala, ku Branham Tabernacle ku Jeffersonville, ndipo gulu la anthu limenelo ndilomvana." Chinachake chikachitika.

⁷⁸ Chabwino, onani zimene Iye amatichitira mu khalidwe lomwe tirimoli, nanga Iye angachite chiyani titakhala a mtima umodzi ndi chimvano? Ndipo njira yokha yomwe tingachitire zimenezo, ndi pakukhala ogwirizana mitima palimodzi ndi chikondi cha pa abale, kumvera a paudindo mu mpingo ndi m'busa; ndipo m'busa amvere Mulungu; ndiye Mulungu amagwira ntchito kupyolera mwa m'busa, kupyolera mgulu loyang'anira, mpakana mu mpingo, ndi onse palimodzi ngati chimango chimodzi mu Ufumu wa Mulungu. Ndiye Mulungu adzatimva pamene tikhala gulu logwirizana. Musalole china chikusautseni. Musakhumudwe ndi chinthu chirichonse.

⁷⁹ Tsopano, wotere ndiye munthu amene Mulungu anamukonzeratu kuti atenge dziko. Mose anali wathunthu, anali mwamuna wosanyengerera. Ngati panali zokangana ndi zokwiyitsana, ndi zina zotero, iye analibe psyete. Ndi zimene Mulungu akutifunira ife tsopano.

⁸⁰ Farao anafuna kuvomereza, anati, "Mose, inu nonse mukhoza kupita, koma musiye ana anu mmbuyo, kapena musiye ng'ombe zanu mmbuyo kuno."

⁸¹ Umo ndi momwe Mdierekezi amafunira kuti M'khristu azidza. "Zidzakhala bwino kuti inu mujowine mpingo, koma musadzamukhululukire Jones. Kudzakhala kwabwino ngati mutabweretsamo zanu...ngati mutapita...Inu simuyenera kusiya kusuta kwanu, kumwa kwanu, kunama kwanu, kuba kwanu. Kufuna kupeza zifukwa kwanu, miseche, simuyenera kuleka zimenezo. Ingojowinani mpingo."

⁸² Koma Mose sanali wapsyete, iye ankafuna chiombolo chathunthu. Iye anati "Sitisiya ng'ombe imodzi kumbuyo. Titenga chirichonse chimene chiri chathu, pamene tikupita kukapembedza Ambuye."

⁸³ Umu ndi momwe mpingo uyenera kukhala uli. "Titenga chilungamo, titenga chiyero, titenga Mzimu Woyera, titenga gulu logwirizana, pamene tikupita pa guwa. Tikhala gulu lenileni, sitisiya kalikonse m'mbuyo. Titenga chirichonse. Sipakhala phazi la ng'ombe limodzi lotsala kumbuyo kuno." Mukudziwa, ndipo anthu akhoza kupemphera mwakuti mpakana Mdierekezi afika polephera.

⁸⁴ Umo ndi momwe Mose ndi gulu lake anachitira. Anafika kumeneko nakhala pansa pa mwazi. Inu munawona, mpaka pamene iwo anakhala pansa pa mwazi panalibe chiwombolo chathunthu. Mose, iyemwini, anali mu umodzi ndi Mulungu. Koma Israeli ayi, anali akanali ndi tchimo, ndipo

ankang'ung'uza motsutsa Mose, ndipo iwo anati “Chifukwa, chifukwa chiyani ukuchita zimenezi? Utibweretsera mavuto ambiri pa ife,” chifukwa Farao anali atangochulukitsa pawiri muyeso wa njerwa ndi zina zotero. Ameneyo anali Mose; iye anali wathunthu m'manja mwa Mulungu, atachotsedwa kwathunthu koweta nkhusa, kuti akawete nkhusa za Mulungu. Iye anali woomboledwa kwathunthu, mwiniwakeyo; koma anthuwo sanali owomboledwa, chifukwa panali kung'ung'uzabe pakati pao.

⁸⁵ Usiku wina pamene Mulungu anakhazikitsa kuti mwanawankhosa aziphedwa, moyimira Khristu, ndipo udzu wa hisope umaviikidwa mu mwaziwo, umene uli udzu (wawamba, wonyozeka), ndi kupaka pa mphutu ya chitseko, ndi m'mbali mwake, ndipo pamenepo ndi pomwe Israeli anawomboledwa kwathunthu, popanda phazi la ng'ombe lotsalira m'mbuyo. Zonse zimene zinali zawo zinawomboledwa. Mabanja awo, okonedwa awo, ndi chirichonse zinaomboledwa pamene iwo anadza kwathunthu pansu pa mwazi.

⁸⁶ Ndipo pamenepa ndi pomwe mpingo uti udzakhale woomboledwa kwathunthu, pamene chirichonse chidza pansu pa Mwazi. Pamene machimo anu abwera pansu pa Mwazi, pamene kusuta kwanu, pamene kutchova juga kwanu, pamene ukamberembere wanu, pamene kuba kwanu, pamene kunama kwanu, pamene zonse zikubweretsedwa pansu pa Mwazi, ndiye padzakhala kuwomboledwa kwathunthu. Ngati wamulakwira winawake, pita ukachikonze. Siungabweretse chimenecho pansu pa Mwazi, sichingakhazikike. Siungabweretse chimenecho. Chinachake sichingakulole kuti utero. Pamene iwemwini uli wathunthu, utabweretsedwa kwathunthu pansu pa Mwazi, padzakhala chiwombolo chathunthu. Ndiye udzakhala ndi ufulu wonga umene siunawudziwe ndi kale lomwe, pamene chirichonse chabweretsedwa pansu pa Mwazi, kubweretsedwamo mogonjera ku Ufumu wa Mulungu. Ndiye padzakhala kuomboledwa kwenikweni.

⁸⁷ Yesu anali kwathunthu, munthu kwathunthu. Iye ankakhoza kulira monga munthu, Iye ankakhoza kudya monga munthu, Iye ankakhoza kukhala monga munthu. Iye anali kwathunthu, munthu wathunthu mmangidwe a thupi Lake. Ndipo, mu Mzimu Wake, Iye anali kwathunthu; Mulungu wathunthu, koteru Iye anachititsa thupi Lake kumvera Mzimu umene unali mwa Iye. Mukuona, Iye anayesedwa mwa njira zonse monga ife. Iye anali munthu, osati Mngelo. Iye anali munthu! Anali ndi zokhumba ndi mayesero chimodzimidzi ndi momwe ife tichitira. Baibulo limati Iye anachita. Iye anali munthu, osati M'ngelo amene sangayesedwe. Ahebri 1 anati kuti Iye anali; Ahebri 1:4 amati Iye anapangidwa mochipetsedwa koposa Angelo. Iye anali munthu, munthu kwathunthu, kuti Mulungu anatenga munthu wathunthu kuti abweretse chiombolo chathunthu;

ndipo anamudzaza Iye ndi Mzimu Wake; Mzimu Woyera unali mwa Iye mopanda muyezo. Ndipo Iye anayesedwa monga ifenso. Ndipo Iye anali Mulungu wathunthu. Iye anatsimikizira zimenezi pamene Iye anadzutsa akufa, pamene Iye anatontholetsa chirengedwe, nyanja yokalipa ndi mphepo zamphamvu. Pamene Iye analankhula kwa mitengo, ndi zina zotero, izo zinamumvera Iye. Iye anali Mulungu, mkatimo. Ndipo Iye akanakhoza kukhala munthu, pakuti Iye anali Munthu, koma Iye wathunthu ndi kwathunthu anadzipereka Iyemwini (ngati Munthu) m'manja a Mulungu, ku ntchito ya Mulungu.

⁸⁸ Ndipo Iye ndi chitsanzo chathu. Ife ndife amuna ndi akazi. Ifenso ndi Akhristu. Ngati Iye ali chitsanzo chathu, tiyeni nafe tidzipereke kwathunthu m'manja mwa Mzimu Woyera, kuti tikhoze kukhala mzika za mu Ufumu wa Mulungu.

⁸⁹ Iye anali munthu wathunthu, Iye anali Mulungu wathunthu, koma Iye anapereka ziwalo zachilengedwe Chake kwa Zake. . . ndipo ziwalo Zake za thupi, ndi maganizo Ake Omwe, ndi zochita Zake Zomwe, ndi zisamalitso Zake Zomwe, ndipo "Ine ndimachita zokhazo zomwe zimakondweretsa Atate Anga." Ndi zimenezotu. Kuomboledwa kwathunthu kuchokera ku umunthu. Ansembe anadza kwa Iye, anthu otchuka, ndipo anati, "Rabbi *Wakuti-wakuti*," nayesa kumunyengerera Iye kuti aziyanjana nawo ndi madinomineshoni, koma Iye anali woomboledwa kwathunthu chifukwa Iye ankadalira mwa Mulungu.

⁹⁰ Kodi Wamasalimo sanati, "Inu mudzamupereka Iye, chifukwa Iye wadalira kwathunthu mwa Ine?" Mukuona? "Ine ndidzamuombola Wokonedwa wanga kwa agalu, chifukwa Iye wandidalira Ine."

⁹¹ Ora lina pamene titi tifike pamapeto a ulendo wa moyo, ine ndikufuna ichi chikhale kwa ine, ndikudziwa inu mukufuna chikhale kwa inuyo. Ine ndikufuna kuti Iye anene, "Ndidzamuombola Iye mu nsagwada za imfa, pakuti iye wadalira mwa Ine. Ndidzamuutulutsa iye m'manda, m'mawa wa chiukitsiro, kumuombola Iye kwathunthu, zonse moyo, thupi ndi Mzimu, chifukwa iye wadalira mwa Ine."

⁹² Ntchito zonse za Yesu zinali zathunthu, chirichonse chinali chathunthu, kwathunthu, chowomboledwa. Iye anawombola kwathunthu wakhate ku makate. Iye anamuombola kwathunthu mkazi wa nthenda ya magari ku matenda akewo. Iye anaombola kwathunthu dziko w tchimo, pamene Iye anafa pa tsiku la chitetezero. Iye anaombola kwathunthu ku tchimo lililonse. Iye anaombola mpingo. Kotero palibe chifukwa choti ife tizikhala ngati anthu opanda chodalira. Palibe chifukwa choti ife tizikhala mogonjetsedwa, chifukwa Iye anagonjetsa Mdierekezi natenga ulamuliro wonse ndi mphamvu naziika pansu pa mapazi Ake, ndipo izo zilibenso chilolezo choti zizilamulira pa inu. Ndife Akhristu, odzazidwa ndi Mzimu Woyera. Sikoyenera kuti Mdierekezi azitiwuza zochita. Khristu anatiombola ife,

chiombolo chathunthu; anatiombola ife ku zoipa, anatiombola ife ku tchimo, anatiombola ife ku zizolowezi, anatiombola ife ku zolongolola, anatiombola ife ku—ku zolaula, anatiombola ife ku mitundu yonse ya zinthu zonyansa. Iye anatiwombola ife kwathunthu ndi kutiyika m'manja Ake ojera, kwathunthu, chiombolo chathunthu.

⁹³ Iye anaombola matenda athu. Iye anatiombola ife ku kudwala, pakuti tiri ndi zikalata za umwini ku zimenezo. Aleluya! “Pakuti Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Iye ndi Mchiritsi wathu. N'chifukwa chake kamkazi kovutika ndi kopuwala kaja, poyesetsa kusamalira mwamuna wake amene anali pafupi kufa ndi khansara, iye anayenda mpaka mkati mwa Pamaso pa Mulungu. Iye anali ndi chikhulupiriro, ndipo iye . . . Madotolo anali atachita zonse zimene akanatha kuchita, kotero iye anatsata malangizo a Mulungu ndipo anawomboledwa kwathunthu.

⁹⁴ Atumwi anali ndi chiombolo chathunthu, chiombolo chathunthu mwa mtheradi. Motani? Chifukwa iwo anali mwathunthu ndi kwathunthu odzazidwa ndi Mzimu Woyera. Pamene uli membala wa mpingo chabe ndi kugwirana chanza ndi m'busa, kapena wina . . . unali ndi za mtundu wina zimene zinakuchitikira za kudumpha, kufuula, kapena kulankhula mmalirime, kapena china chinzake; nukhalabe uli ndi chiwembu mumtima wako, machitidwe achilendo, kunena bodza, kusuta fodya, kukhumbira akazi; pali china chimene sichinachitikebe, pali china cholakwika, “pakuti iye amene akonda dziko kapena zinthu za mdziko, chikondi cha Mulungu sichiri mwa iye.” Iwe wasoheretsedwa. “Ndi zipatso zawo mudzawadziwa iwo.”

⁹⁵ Iye tonse tikufuna kugwirizana limodzi ndi Mzimu Woyera. Membala aliyense ayenera kugwirizana ndi mzake. Chikondi cha Mulungu chafalitsikira m'mitima yathu ndi Mzimu Woyera, Iwo ukutitsuka ife ku zosalungama zonse, tawomboledwa ku zinthu za mdziko. Yesu anati, “Ndi ichi anthu onse adzadziwa kuti inu muli ophunzira Anga, pamene mukondana wina ndi mzake.” Pamene membala wina akonda membala mzake kwambiri mwakuti akhoza kulola kuferana.

⁹⁶ Pamene chinthu chimodzi choyipa chiyamba, dziko la kunja, tiakazi tina tikhoza kudza, nititi, “Tsopano taonani, okonedwa, zikanakhala bwino ukanachita *izi* kapena kuchita *izo*, ukanavala *ichi* kapena kuchita *icho*, kapena ukanachita *ichi* nuchoka mu gulu la anthu osokonezeka aja, kapena zina zonga zimenezo.”

⁹⁷ Iye ndife ogwirizana kwambiri ndi Mulungu! Inu mukuti, “Chabwino M'bale Branham, ndi yesero lovuta” Koma Khristu anafera cholinga chimenecho. Mdierekezi wagonjetsedwa. Iye tikufuna chiombolo chathunthu. Iye tikufuna mpingo umene uli wangwiro ndi wachiyero ndi wasasakanizidwa, ndi

wotsukidwa mu Mwazi wa Mwanawankhosa, ndi odzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi] . . . kuombola aliyense mwathunthu. [Malo opanda kanthu pa tepi.]

⁹⁸ Mulungu Wokodedwa, Inu simumatenga zinthu pokha ngati ziri zowomboledwa kwathunthu. Inu simungalandire nsembe yomwe ili ndi chilema pa iyo. Inu simungalandire pemphero lomwe liri ndi tchimo mkati mwa moyo wa munthu ameneyo. Inu simungachite nkomwe, Ambuye. Inu simunazichitepo mu mibadwo yapitayo, ndipo Inu simungazichite lero. Koma nsembe ikhale yopanda chirema. Ndipo, Ambuye Mulungu, pamene tikudzigoneka tokha paguwa ngati miyoyo yoperekedwa, tichotsereni ife, O Ambuye, zirema zonse za tchimo. Ine ndigoneka moyo wanga kwathunthu ndi thupi langa ndi mphamvu zanga ndi kulimbikira kwanga, ndi mpingo uwu mmawa uno, pa guwa. Tiyeretseni ife ndi Magazi Anu, ndi kutikhululukira ife tchimo lililonse limene tinalichita. Ndipo mulole Mzimu Woyera wopambanawo ukhale pa ife mwakulemera, ndi Kukhalapo Kwake kupite nafe kuchokera mu kachisi uyu mmawa uno, kuti tidziwe mkati mwathu kuti Iye watikhululukira ife. Ndiye pemphero likhala loti, “Tikhululukireni ife zolakwa zathu monga ife tikhululukira amene atilakwira.” Tichitireni, Ambuye.

⁹⁹ Khalani Inu pafupi nafe tsopano, tidalitseni ife ndi kutisunga mpaka tidzakumanenso pa msonkhano wa usiku uno. Mulole kuti tikabwere ndi manja oyera ndi mtima wangwiwo, kuti Inu musatisiye, pakuti ife tikufuna mwathunthu kuwomboledwa kwathunthu ku chirichonse, Ambuye, chomwe chingatilepheretse ife kukhala kuwala kwa dziko; nyali yomwe yaikidwa pamwamba pa phiri, osati mbiya itavindikira pa iyo, koma nyali yomwe yaikidwa pamwamba pa phiri, imene ikupereka kuwala kuti ikalondolere mapazi a anthu mu njira yomwe ili yolondola. Tipatseni, Atate. Tikupempha izi mu Dzina la Yesu, ndi kwa ulemerero Wake. Amen.

¹⁰⁰ Ndimufunsa Doc, ndikuganiza kuti ali kumbuyoko, kapena mmodzi wa madikoni amene alipo, kuti mpingo uziwerenga izi. Doc, bvera ukayike ichi powerengerapo zochitika kuti mpingo ukhoze kumazona pamene akutuluka. Ndipo pamene M’bale Collins, ngati ali pano . . . Kodi M’bale Collins ali muno? Mpatseni iye chinachi.

¹⁰¹ Chabwino, bwana, ndipo tiwona zomwe . . . [M’bale Branham adikira—Mkonzi]. Uyo ndi wina wofuna kulankhulana naye payekha. Izo nthawi zonse zimachitika. Tiri okondwa. Ndipo ndakhala ndikulankhula ndi anthu paokha. Mukuona, chomwe mungachite ndi kungotichitira telefoni nambala yathu uko. Ife—ife tinali ndi vuto lalikulu kunyumba; mwakuti, mpingo ukuzidziwa zimenezo, (uyu ndi mlendo), mpingo ukudziwa za zimenezi. Payenera kukhala kachidziwitso

katayikidwa...Ndikayika kuno mu tchalitchi, nakonso, kwa ongobwera. Mukuona, pali ochuluka kwambiri, mwakuti sitingasamalire onsewo, koma momwe angamadzere mwa manambala. Mwaona? Ndipo ife...Ndipo ngati mutangochitira telefoni ku BUTler 2-1519 BUTler. Ndipo aliyense wa mamembala amene angamuone wina amene akufuna...Ine nthawi zonse ndimakonda kuwaona anthu, koma tiri ndi dongosolo lake lolitsata. Pali ena amene anayitanidwa kale, angapo, onani, ndipo timangobwera mwa mmodzi ndi mmodzi pamene tikudza. Ndiye pali...Poyamba tinkangochita mwachinawamba, muli monse, kudumpha, kujowa, anthu ankapita kwao ali okhumudwa ndi chirichonse. Tsopano ali ndi chirichonse mwa dongosolo. Ndipo ndi chomwe tikuyesa kulankhula za icho tsopano, onani, kuyika chirichonse mu dongosolo, mwangwiro bwinobwino. Ndipo ndidzakondwera kuona mzathu wokonedwayu, ngati ati adzangochitira telefoni ku BUTler 2-1519, -1519, ndipo a Mercier kapena a Goad, mmodzi, adzayankha foni nakuwuzani kwenikweni kuti tingadzakumane liti. Tiri ndi malo kumeneko, muli makina opereka mpweya wabwino, ndi mokonzedwa kale koyenera kulandiriramo anthu ndi kuwapempherera. Ndife okondwa kokha pakuchita izi.

¹⁰² Tsopano, chifukwa chomwe sindimadza ku tchalitchi, anthu amaganiza kuti ndikuyesa kuthawa anthu, sichoncho ayi. Ndikuyesa ku—kukhala mdongosolo kwenikweni. Onani, icho ndi chifukwa chomwe ndikufunira kukhala, kuti ndisamasonyeze kukondera kwa anthu ena. Munthu aliyense, wina aliyense, kulikonse, nthawi iriyonse, onani; khungu, chiphunzitso ziribe chochita pa izi. Timabwera kumeneko nitidzakumana ndi anthu. Ndipo, ngati ali ndi chosowa, timakhala pomwepo ndi Ambuye mpaka chitakonzeka. Ngati akufuna kudziwa chirichonse cha misonkhano, ndithu, timasamalira zimenezo ndi kuziyika limodzi ndi zinzake, umo ndi mwa kutsogolera kwa Mzimu Woyera kokha. Ndipo iyo ndiyo njira yake, ndikuganiza kuti ndicho chilungamo, zimamuchitikira aliyense chimodzimidzi. Kotero, palibe kukondera munthu, palibe kukondera.

¹⁰³ Kodi panali anthu ena alionse amene anadza kudzapemphereredwa mmawa uno, amene ali odwala ndipo amafuna kupemphereredwa? Chabwino, palibe? Ndiye tiyeni tiyimbe kanyimbo kabwino ka...kopembedzera. Tingayimbe chiyani mmawa uno? “*Ndi chiani chomwe chingachotsere machimo anga?*” Mukuidziwa imeneyo, Teddy? “*Palibe china koma Mwazi wa Yesu.*” Ndi chiani...[Mlongo mu mpingo akufotokoza za mlongo amene ali “wodwala kwambiri”—Mkonzi]. Chabwino, mlongo. Mukufuna timupempherere pakali pano? Ndimupempherera mlongoyo. Kusanjika manja pa mkazi uyu *apa*. Kodi mungaweramtse mitu yanu nane kwa kamphindi, mwa kachetechete tsopano.

¹⁰⁴ Mulungu Wokonedwa, pali mkazi amene ali wodwala kwambiri. Mlongo wathu wayika thupi lake pamwamba...?... ngakhale kutenga khansara kuchokera kwa ena, wawayimira pakati ena. Koma Inu mumuwombole kwa izo, Ambuye. Masiku angapo apitawo pamene zinthu izo zinadziwika, muloleni naye azindikire zimenezi yekha chotero, Ambuye, iye adziwa kuti zimachokera kwa Inu. Ine ndikusanjika manja anga pa iye ndi kufunsa chifundo kwa mkazi winayo. Lolani chisomo cha Mulungu, mphamvu ya Mzimu Woyera...?... mitima yathu, Ambuye. Wululirani ichi kwa ife poyamba...?... Ndiye tidziwa kuti tapeza chifundo ndi Mulungu, tiri nawo mtendere ndi Mulungu, tilandira chomwe tapemphera, chifukwa tiribe chotitsutsa. Tichitireni, Ambuye. Mu Dzina la Yesu ndipemphera. Amen. Zikomo, mayi. Chabwino.

Nchiani chinganditsukire tchimo langa?
Sichina koma Mwazi wa Yesu;
Nchiani chomwe chingandichiritsenso?
Sichina koma Mwazi wa Yesu.

O, chitsime chofunika
Chomwe chindiyeretsa ngati chipale;
Palibe kasupe yemwe ndikumudziwa,
Sichina koma Mwazi wa Yesu.

¹⁰⁵ Ndi angati amene mukumva kuti machimo anu ali pansu pa Mwazi? Tiyeni tiyiyimbe ndi manja athu tsopano.

Nchiani chinganditsukire tchimo langa?
Sichina koma Mwazi wa Yesu;
Nchiani chomwe chingandichiritsenso?
Sichina koma Mwazi wa Yesu.

Tsopano pamene tikugwetsa manja athu, tiyeni tigwirane chanza ndi a pafupi nafe.

Chitsime chofunika
Chomwe chindiyeretsa ngati chipale
Palibe kasupe wina amene ndikumudziwa,
Sichina koma Mwazi wa Yesu.

Kodi inu mumamukonda Iye?

O, momwe ndimkondera Yesu,
O, momwe ndimkondera Yesu,
(Tsopano pitirizani nayo, aliyense gwiritsani
kwa Mulungu)

Momwe ndimkondera Yesu,
Chifukwa Iye anandikonda poyamba.

Sindidzamusiya yekha Iye.



KUOMBOLEDWA KWATHUNTHU CHA59-0712
(A Total Deliverance)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi pa Lamlungu mmawa, Julaye 12, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©1992 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org